

# Banja laling'ono, umoyo wathanzi mboma la Ntcheu

## Banja la anthu ochepa limapindula mokwanila kuchokela ku zithandizo zosianasiyana za mdziko zokhudza miyoyo yavo.

- Mu zaka makumi awiri zapitazi chiwerengero cha anthu mboma la Ntcheu chakula ndithu koma mosapitilira theka kuchoka pa anthu 105 kufika pa anthu 138 pa km<sup>2</sup> ili yonse.
- Nyumba zokhala anthu zisanu ndi imodzi (6) mwa nyumba zisanu ndi ziwiri (7) zili zonse zili ndi potunga madzi a ukhondo pa makono.



Nyumba zokhala anthu zisanu ndi zinayi (9) mwa nyumba khumi (10) zili zonse zimagwilitsa ntchito nkhuni pophika; ndipo nyumba zinayi (4) zokha mwa nyumba zana-limodzi (100) zili ndi magetsi.



Amayi awiri (2) okha mwa amayi makumi khumi (100) aliwонse; komanso abambo anayi (4) mwa abambo makumi khumi (100) aliwонse ndi amene amamaliza maphunziro awo a ku sekondale.

- Amayi atatu (3) mwa amayi anayi (4) aliwонse komanso abambo anayi (4) mwa abambo asanu (5) aliwонse amadziwa kulemba, kuwelenga ndi kuwelengera.
- Amayi khumi ndi anayi (14) mwa amayi makumi khumi (100) aliwонse komanso abambo asanu ndi mmodzi (6) mwa abambo makumi khumi (100) aliwонse sali pa ntchito iilyonse yolembedwa.
- Amayi atatu (3) mwa amayi anayi (4) aliwонse amavutika kwambiri kupeza chithandizo cha mankhala akadwala chifukwa zipatala zoyandikila ndi kumene amakhala zili kutali kwambiri.

### Ubwino wotsatira njira za kulera

Banja likakhala ndi ana ochepa, zimathandiza makolo a anawa kuaphunzitsa mokwanila ana awo chifukwa choti aphunzira bwino, anawa amakhala ndi mwaiy wopeza ntchito zabwino mtsogolo. Kuchepetsa kachulukidwe ka anthu mdziko kumathandiza boma ndi mabungwe othandiza boma kukonzekera bwino pa ntchito zopititsa umoyo wa anthu patsogolo monga kukhala ndi madzi a ukhondo, ntchito za umoyo komanso za mtengatenga.

## Banja la anthu ochepa limakhala ndi mayi wa moyo wathanzi komanso banjalo limakhala losangalala



Amayi amabeleka ana asanu (5) kapena asanu ndi mmodzi (6) pa moyo wawo wonse koma amaonetsa chidwi chobeleka ana anayi kapena asanu wokha pa moyo wao wonse.



Amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwонse a zaka za pakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zinayi (19) ayamba kale kubeleka ana.

- Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwонse amabeleka kunyumba osati kuchipatala.
- Amayi awiri (2) mwa amayi asanu (5) aliwонse omwe ali pa banja amatsata njira za kulera; ndipo amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwонse amatsa njira zolererazi kuti asabeleke ana ambiri.
- Amayi asanu ndi atatu (8) mwa amayi makumi khumi (100) aliwонse komanso abambo khumi ndi awiri (12) mwa abambo makumi khumi (100) aliwонse amakhulupilira kuti ndi zovomelezeka kuti mamuna akhoza kumenya mkazi wake nthawi zina.

### Ubwino wotsatira njira za kulera

Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwонse a zaka zapakati pa khumi ndi zasanu (15) ndi makumi anayi ndi zisanu ndi zinayi (49) amamwalira pa nthawi yobeleka mwana. Kutsatila njira za kulera kumathandiza amayi omwe ndi achichepeleko kutenga nthawi asanakhale ndi mimba (pathupi) ndipo kutenga nthaw chonchi kumathandiza kuti asapeze mavuto mthupi mwavo omwe amadza chifukwa chobeleka akadali ang'ono. Amayi ngati akhala ndi ufulu wosankha nthawi yoti abelete komanso kusyanitsa zaka za ana obelekedwa zimawathandiza kuti akhale ndi moyo wathanzi. Ana omwe amayi awo anamwalira nthawi zambiri samamaliza maphunziro awo ku sukulu.

## Banja la anthu ochepa ana ake amakula bwino komanso amakhala ndi moyo wathanzi

- Mwana mmodzi (1) mwa ana asanu (5) aliwонse wochepera zaka zisanu (5) amakhala ndi thupi lopelewela losagwilizana ndi msinkhu wawo.




Ana awiri (2) mwa ana asanu (5) aliwонse wochepera zaka zisanu (5) amakhala wopinimbira.

### Ubwino wotsatira njira za kulera

Kutsatila njira za kulera kumathandiza ma banja kuti ana awo akule ndi moyo wathanzi komanso kutha kuonetsetsa kuti pakupita nthawi yokwanila bwino pamene mwana wabada ndi nthawi yomwe mwana wina akudzabdawano mbanjamo. Ana obadwa mosiyana ndi zaka zitatu kapena kupitilira apo amakhala ndi mwaiy wokhala moyo wochuluka kwambiri kuposa ana omwe abadwa mosiyana ndi zaka ziwiri kapena kuchepela apo. Makolo omwe ali ndi ana ochepa amasamalira bwino ana awo ndi kuwapatsa zakudya zokwanila.

Anthu awiri mwa anthu atatu aliwонse mbomali ali ndi zaka zosapitilira makumi awiri ndi zisanu (25)

Zaka



Source: National Statistical Office of Malawi, Population Projections Malawi.



Mdziko la Malawi, amayi amodzi amamwalira pobeleka ana pa ma ola awiri aliwонse.



Mwana wakhanda mmodzi wosakwana chaka chimodzi amamwalira ma ola asanu ndi limodzi aliwонse.



Pa ma ola atatu aliwонse mwana mmodzi wosakwanitsa zaka zisanu amamwalira.